



EXAMINATION NO.: _____

THE MALAWI NATIONAL EXAMINATIONS BOARD

2023 MALAWI SCHOOL CERTIFICATE OF EDUCATION EXAMINATION

CHICHEWA

Subject Number: M032/II

Tuesday, 11 July

Time Allowed: 2 hours

1:00 – 3:00 pm

PAPER II

(Malikisi 90)

Malangizo:

1. Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi ndi anayi
2. Pepalali lili ndi magawo anayi: A, B, C ndi D.
3. Lembani nambala yanu yamayeso pamwamba pa tsamba lililonse la pepalali.
4. Muchitebulo chili pambalichi, onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.
5. Perekani pepalali kwa oyang'anira mayeso nthawi ikakwana.

Funso	Chongani funso ngati mwayankha	Muno musalembemo	
1			
2			
3			
4			
5			
6			
7			
Total			

Gawo A (Malikisi 40)**Malamulo a Chiyankhulo.**

Langizo: Yankhani mafunso **onse** m'gawo ili pa mizere ili pansi pa funso lililonse.

1. a. Kodi aneni omwe ali ndi mzere kungsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi ali mu kachitidwe kanji ka aneni?
- (i) Ine ndipita nawo kwanuko.
_____ (Malikisi 1)
- (ii) Nandolo wadyedwa kale.
_____ (Malikisi 1)
- (iii) Zomwe mwafotokozazo zamveka.
_____ (Malikisi 1)
- (iv) Wakubayo wamangwa.
_____ (Malikisi 1)
- (v) Mwanayu amachita chipongwe.
_____ (Malikisi 1)
- b. Perekani zambiri za mayina otsatirawa:
- (i) gang'a _____ (Malikisi 1)
- (ii) sukulu _____ (Malikisi 1)
- (iii) nzimbe _____ (Malikisi 1)
- (iv) cheke _____ (Malikisi 1)
- (v) dzino _____ (Malikisi 1)

Mafunso akupitirira/...

2. a. Tchulani mitundu ya ziganizo zotsatirazi.

(i) Mary walembe mayeso.

(Malikisi 1)

(ii) Iwo adapita ndipo adayenda bwino.

(Malikisi 1)

(iii) Ndizoona kuti wakhoza mayeso.

(Malikisi 1)

(iv) Ngakhale anabwera kwathu, iye sanandipeze chifukwa ndinali nditachokapo.

(Malikisi 1)

b. Lembani ziganizo zomveka bwino zosonyeza aphantikiram'tsogolo amene akugwira ntchito zotsatirazi ndipo mutseke mzere kungsi kwa aphantikiram'tsogolowo.

(i) kubwereza

(Malikisi 2)

(ii) kutsimikiza

(Malikisi 2)

(iii) kulemekeza

(Malikisi 2)

3. Tchulani mitundu ya nthambi zosaima pazokha zomwe zili ndi mzere kungsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi ndipo mutchule ntchito zawo.

- (i) Zimene wabweretsazo sizinandisangalatse.

Mtundu : _____ (Malikisi 1)

Ntchito: _____ (Malikisi 1)

- (ii) Imodzi yomwe yasowayo ndi yanga.

Mtundu : _____ (Malikisi 1)

Ntchito: _____ (Malikisi 1)

- (iii) Iye adayamba kudandaula atatsala pafupi kufika.

Mtundu : _____ (Malikisi 1)

Ntchito: _____ (Malikisi 1)

- (iv) Mukandidikire pomwe mukapeze njira zitatu.

Mtundu : _____ (Malikisi 1)

Ntchito: _____ (Malikisi 1)

- (v) Ichi ndi chimene chandivutitsa usiku onsewu.

Mtundu : _____ (Malikisi 1)

Ntchito: _____ (Malikisi 1)

4. Phwanyani chiganizo chili m'munsimu pounika mawu paokhapaokha.

Ana akusewera.

(Malikisi 10)

Gawo B (Malikisi 20)

Kumvetsa Nkhani ndi Kusanthula Chiyankhulo

5. Werengani nkhani ili m'munsiyi mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawo pa mizere ili pansi pa funso lililonse.

Misozi adali mwana woyamba kubadwa m'banja la Bambo ndi Mayi Ganizani. Mtsikanayu adakula ndi moyo wathanzi ndipo adali wochititsa kaso kwa aliyense. Ali pamsinkhu wopita kusukulu, makolo sadachite bowa bwanga, koma kumuyambitsa mwanayo sukulu. Adampititsa pasukulu ya Kathebulu. Ali m'makalasi oyambirira, Misozi adalumira mlomo wakunsi pomwa inki pozindikira kuti zokoma zili m'tsogolo. M'mudzi wa Chambuzi mudalibe mwana amene ankamaliza maphunziro ake. Ambiri ankangolekezera makalasi ang'onoang'ono monga mu sitandade 3 ndi 4. Ngati mwana wina walimbikirako, ankathera mu sitandade 6. Kunena zoon, udali mudzi womvetsa chisoni chifukwa udadzadza ndi anthu osaphunzira.

Mafunso akupitirira/...



5. (Continued)

Zinthu zidachita chenjerere pomwe Misozi adathyola bano. Amayi ambiri a m'mudzimo adayamba kumulangiza zoti asatayenso nthawi ndi zasukulu chifukwa zimuchedwetsa. Misozi atadya mutu pa malangizowa, adatemetsa nkhwangwa pa mwala kuti sasiya sukulu. Anzake anthanga imodzi ndi iye adayamba kumusala chifukwa cha chisankho chake chopitiriza sukulu. Panthawiyi n'kuti ali mu sitandade 7. Anzake ambiri adali atachembeza kamodzi kapena kawiri. Misozi adanyansidwa ndi makhalidwewa kotero kuti adaganiza zoti achoke kumudziko ndi kupita kukakhala ndi abale ake kutauni.

M'mawa watsiku lina, Bambo Ganizani adaitanitsa mwana wawo Misozi ndi kumulangiza motere, "Mwana wanga, tsopano wakula, sindiyenera kumakulonda kapena kukuuza zochita. Ona anzako anthanga imodzi ndi iwe ali ndi ana. Iwe watani, mwina ndiwe chumba kapena phale? Mmene ndimakuonera ine, mwana wanga ndiwe njole yeniyeni yochititsa ngozi amuna pamsewu akukuyang'ana. Bwanji sugwiritsa ntchito mwayi wakukongola kwako kuti undipezere mkamwini komanso zidzukululu?"

Misozi adamvetsera mawu onse omwe bambo ake adayankhula. Iye adayankha nati, "Bambo, zikomo kwambiri chifukwa cha malangizo anu. Ine zaukwati pakadali pano zili kunkhongo. Ine mwamuna wanga ndi ana anga ndi maphunziro basi. Chomwe ndingapemphe kwa inu pakadali pano ndi chilolezo choti ndipite kutali kuti ndikapitirize maphunziro." Bambo ake adamulola ndipo adamutumiza kwa m'bale wawo kutauni ya Tchemba.

Misozi adasangalala kwambiri atachoka kumudzi kwawo kuti akapitidweko mphepo zina kutauni. Ali kumeneko, adachirimika mpaka kupambana. Adasankhidwa kupita ku sekondale ya Tchemba. Sukuluyi idali yoyendera.

Mafunso akupitirira/...

5. (Continued)

Misozi adalimbikira kwambiri maphunziro ake kuti m'tsogolo adzakhale chitsanzo cha mudzi wa Chambuzi. Atalemba mayeso a Fomu 2, adasankhidwa kukayamba Fomu 3 pasukulu ina yogonera komweko yotchedwa Katolonji. Apa Misozi adadziwa kuti kanthu n'khama phwiti adakwatira njiwa. Choncho sadabwerere m'mbuyo pa maphunziro ake. Aphunzitsi apa Katolonji adamukonda chifukwa cha luntha lake m'kalasi.

Adalemba mayeso a Fomu 4 ndipo zotsatira zitatuluka, zidaonetsa kuti adakhoza bwino kwambiri kupambana atsikana anzake ndi anyamata ambiri. Misozi adali ndi lingaliro loti akachite maphunziro aukachenjede okhudza kusasiyanitsa pakati pa amuna ndi akazi. Izi zidathekadi chifukwa adasankhidwa kukapitiriza maphunziro ake ku yunivesite ya Ulalo.

Misozi adakhala ku yunivesite ya Ulalo zaka zinayi akuzamitsa ukadaulo pa maphunziro aatsikana. Atamaliza maphunzirowa, sadafune kulembedwa ntchito koma adasankha kuyambitsa bungwe lake lothandiza pa maphunziro aatsikana. Bungwe lake adalitchula Tiwoloke ndipo lidatsegulidwa m'madera ambiri. Iye adalemba ntchito achinyamata ambiri m'bungweli.

Tsiku lina Misozi adaganiza zokaona makolo ake kumudzi kwawo chifukwa padali patatha zaka khumi chichokereni. Adanyamuka pa galimoto yake kuwuyatsa wa kwawo. Adagula zinthu zambiri zokapatsa makolo ndi abale ake.

Misozi atafika kumudzi kwawo, chomwe chidadulitsa mutu wazizwa ndi choti adaona anzake atakalambiratu. China chomwe chidamudodometsa ndi choti galimoto yake ikufika pakhomo pa makolo ake, anthu ambiri adayamba kuthawa poganiza kuti kwabwera akuba kapena achifwamba. Ena olimba mtima adaona mayi wosalala kwambiri komanso wokongola akutsika galimoto zomwe zidali

Mafunso akupitirira/...

5. (Continued)

zachilendo pamudzipo. Anthu adali suzisuzi kuti mwina angamudziwe munthu amene adatsika galimotoyo. Ayi ndithu, palibe adaloserako ngakhale kuganizirako za Misozi.

Misozi adamva chisoni ataona makolo ake ali mu umphemvu m'dyera kumthiko wadzaoneni. Pamene ankatuluka m'kakhumbi kawo atadzadzidwa ndi mantha, poona mlendoyo akulunjika kwa iwo, mayi ake ndi amene adamuzindikira ndi kuitana, "Misozi! Mwana wanga, takulandira!" Bambo Ganizani adaimirira n'kuseleula, "Dziko limakondera ili, n'zoonadi sayenda adabala mwana adayenda, ndiwedi mwana wanga Misozi?" Uku kudali kulandiridwa kwa Misozi pakomo pa makolo ake chichokere zaka khumi zapitazo.

Misozi adasangalala kukhala pakati pa abale ndi anansi ake kwa masiku atatu. Makolo a m'mudzimo adachita kaduka ndi maonekedwe a Misozi kotero kuti adayamba kunena zinthu zambiri zomupitsa. Ena ankati munthu wamkulukulu wopanda mwamuna, ndiye sukulu yake ndiyo imukwatire? Ena ankati makolo ake ndi afiti, bwanji ana awo sadaphunzire ndi kulemera? Ngakhale zoyankhula zidali zosaneneka panthawiyi, Misozi sadazitengere ndipo adangoziponya kunkhongo.

Misozi adapereka mituka yosiyanasiyana kwa makolo ndi abale ake m'mudzi muja. Iye sadawerengere mfunda kaya chimvano chawo pamudzipo. Chomwe adadziwa iye ndi choti kutengezana denga lowola n'kuchulukana manja. Kwa iye kunali kuthokoza chifukwa adafika pomwe adalipo chifukwa cha makolo ndi abale ake.

Misozi adakhazikitsa ofesi yoona za maphunziro aatsikana m'mudzi mwawo muja. Anthu onse m'mudzimo komanso m'dera lonse lakwawo adailandira ofesiyo ndi ntchito zake. Izi zidachititsa kuti maphunziro aatsikana apite patsogolo m'deralo.



5. (Continued)

- a. (i) Kodi Misozi adali mwana wachingati pobadwa?

(Malikisi 1)

- (ii) N'chifukwa chiyani mudzi wa Chambuzi udali womvetsa chisoni?

(Malikisi 2)

- (iii) Tchulani zinthu **ziwiri** zomwe anzake a Misozi adachita nthawi imene iye adali mu sitandade 7.

(Malikisi 2)

- (iv) Tsimikizani kuti amayi a m'mudzi wa Chambuzi adali a makhalidwe oipa.

(Malikisi 2)

- (v) Tchulani zinthu **ziwiri** zomwe Misozi adayankha bambo ake atamuitanitsa ndi kumulangiza.

(Malikisi 2)

- (vi) N'chiyani chidachititsa kuti Misozi akaphunzire ku sukulu ya Tchemba?

(Malikisi 2)

Mafunso akupitirira/...



5. a. (Continued)

- (vii) Tchulani zinthu **ziwiri** zomwe anthu ankamunena Misozi atapita kwawo kuchokera ku tauni.

(Malikisi 2)

- (viii) Kodi mkuluwiko woti “Sayenda adabala mwana adayenda” ukutanthauzanji m’nkhaniyi?

(Malikisi 2)

b. Kusanthula chiyankhulo

- (i) Pezani mawu m’nkhaniyi omwe akufanana matanthauzo ndi awa:

1. nsanje

(Malikisi 1)

2. lidathangata

(Malikisi 1)

3. mphatso

(Malikisi 1)

- (ii) Pezani zining’a m’nkhaniyi zomwe matanthauzo ake ndi awa:

1. mkazi wosabereka _____ (Malikisi 1)

2. kusauka _____ (Malikisi 1)

Gawo C (Malikisi 15)**Chifupikitso**

6. **Werengani nkhani yotsatirayi mosamala. Nkhaniyi ili ndi mawu 140 ndipo muifupikitse kuti ikhale ndi mawu osachepera 45 komanso osapitirira 55.**

Banja la a Manyota lidali ndi ana anayi. Awiri mwa anawo adali anyamata ndipo awiri enawo adali atsikana. Banjalo limakhala mosangalala nthawi zonse poti makolo onse amagwira ntchito. Bambo adali mkulu woyang'anira zachuma pa kampani yopanga shuga pamene mayi adali namwino.

Bambo Manyota adali ndi galimoto ndipo nthawi zonse amaonetsetsa kuti popita kuntchito awatenge akazi awo komanso ana awo kukawasiya kuntchito ndi kusukulu. Kunena zoona, banjali lidali pachinyezi.

Mmodzi mwa ana amuna adachita ngozi. Adathyoka mwendo wake galimoto itamuwomba akuwoloka msewu. Izi zidadandaulitsa aliyense m'banjamo chifukwa adadziwa kuti lungalunga mpobadwa chilema chichita kudza. Aliyense adatengapo mbali posamalira mnyamatayo kotero kuti iye ankakhala mosangalala ngati poyamba.

Chidwi cha aliyense walungalunga m'banjamo chidali pa kusangalatsa mnyamata wolumalayo pofuna kumubweretsera chimwemwe mumtima. Ena amayesetsa kumuchezetsa pamene enanso amamuthandiza m'njira zina. Izi zidalimbitsa mtima mnyamatayo chifukwa ankalandira chikondi chopanda malire kuchokera kwa abale akewo.

Mafunso akupitirira/...

Gawo D (Malikisi 15)

Chimasuliro

7. **Masulirani nkhani yotsatirayi m'Chichewa chomveka bwino.**

CELL PHONES

It is a well-known fact that nowadays, communication has greatly improved with the coming in of cell phones. People are able to reach out to friends and relatives in far away places in the shortest possible time.

Even in villages, many people have cell phones. It becomes very strange, in a group, to find a person who has no cell phone. Apart from communication, people are using cell phones as a source of entertainment. Funny messages, gossips and pictures are sent through cell phones to make others laugh.

Cell phones have also proved to be a source of misfortunes. Disputes have started in families or between trusted friends because of cell phones. Marriages have broken up because of mistrust that has come out from the way partners use their cell phones. It is, therefore, very clear that much as cell phones are very useful in our lives, they can also be a source of evil.

Mafunso akupitirira/...

7. (Continued)

Blank lined paper for writing.

(Malikisi 15)

MAFUNSO ATHERA PANO

NB: Pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi ndi anayi.